-Mulungu amawona mu mtima.

-Mulungu amadziŵa ngati tikukhulupilira mwa Yesu ndi mtima wathu onse, kapena tikungolankhula ndi pakamwa pathu pokha.



# PHUNZIRO LA 54

1. Kodi Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo ankafuna kuwona chiyani m'malo moŵakhulupilira Mawu a Mulungu?
-Ankafuna kuwona chizindikiro chozizwitsa.

2. Kodi chifukwa chiyani Afarisi ndi aphunzitsi a malamulo ankapenpha kuti Yesu aŵawonetse zizindikiro zozizwitsa zambiri?
-Chifukwa chakuti sankakhulupilira kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi.

3. Kodi kuwona zizindikiro zozizwitsa kungatipulumutse ife?
-Iyayi.

4. Ngati tikuganiza kuti tikhoza kukhulupilira M'mawu a Mulungu tikawona chizindikiro chizizwitsa, ndiye kuti tikumutcha Mulungu kuti ndi otani?
-Tikuŵatcha Mawu a Mulungu kuti ndi abodza.

5. Kodi chizindikiro chozizwitsa chimene Yesu anapereka kwa anthu chinali chotani?
-Chizindikiro chozizwitsa cha Yona.

6. Kodi chizindikiro cha Yona chinali chotani?
-Ngati m'mene Yona anakhalira m'mimba mwa chimsomba masiku atatu ndi usiku wache, chomwechonso Yesu adzakhala m'mimba mwa dziko la pansi masiku atatu ndi usiku wache.

7. Kodi chifukwa chiyani Yesu ananena kuti Ayuda ndi oyipa kwambiri kuposa anthu a ku Nineva?
-Chifukwa chakuti anthu a ku Nineva anatembenuka

mitima yawo chifukwa cha chiphunzitso cha Yona koma Ayuda sanatembenuke mitima yawo ndi chiphunzitso cha Yesu, Mulungu Mpulumutsi.

-Afarisi anamuda kwambiri Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani Afarisi anamuda kwambiri Yesu?

-Chifukwa chakuti Yesu anaŵawuza kuti Iye ndi Mulungu Mpulumutsi.

-Farisi ankaganiza kuti Yesu anali munthu ngati anthu ena.
-Ankaganiza kuti palibe munthu wina aliyense amene angathe kudzitcha kuti ndi Mulungu.

-Kodi chifukwa china chimene a Farisi anankamudera Yesu chinali chotani?
-Chifukwa chakuti Yesu anaŵawuza kuti iwo ndi ochimwa, ndipo Mulungu adzaŵalanga ngati satembenuka mitima.

-A Farisi sankakhulupilira kuti iwo anabadwira mu tchimo.
-Ankaganiza kuti sanachimweko m'miyoyo yawo monse.

-Kodi chifukwa china chimene a Farisi anankamudera Yesu chinali chotani?
-Chifukwa chakuti anthu ambiri ankamutsata Yesu, a Farisi ankamuchitira kaduka Iye.

-A Farisi ankaganiza kuti anthu ambiri adziŵamvera iwo m'malo momumvera Yesu.
-A Farisi ankaganiza kuti anthu ambiri adziŵatsatira iwo m'malo momutsatira Yesu.



18-Andireya, Filipo ndi Batolomeyo, Mateyu ndi Tomasi, ndi Yakobo mwana wa Alifeyo, ndi Tadeyo, ndi Simoni Mkanani,
19-ndi Yudasi Isikariyoti, amene anamupereka Iye.

-Mwa anthu amene anamutsatira Iye, Yesu anasankha anthu khumi ndi aŵiri kuti akhale ophunzira ache.
-Anthu khumi ndi aŵiri ameneŵa ankatchedwa kuti Alariki.

-Alariki amene anaŵasankha Yesu sankadziŵa kuŵerenga ndi kulemba bwino, ndipo palibe amene anali ndi ndalama zambiri.

-Yesu anaŵasankha iwo chifukwa chakuti anakhulupilira mwa Iye.

-M'modzi mwa anthu amene Yesu anamusankha anali Yudasi.
-Yudasi ankanena kuti ankamukhulupilira Yesu, koma ankangolankhula zimenezi ndi pakamwa pache pokha.

-Mu mtima mwache, Yudasi sankakhulupilira mwa Yesu.

-Ophunzira a Yesu khumi ndi aŵiriwo sankadziŵa kuti Yudasi sankakhulupilira mwa Yesu koma Yesu ankadziŵa.

-Yesu ankadziŵanso kuti tsiku lina Yudasi adzamupereka Iye kwa adani ache.

-Ife tikhoza kumaŵanamiza anthu kuti tikukhulupilira mwa Mulungu ngati Yudasi, koma sitingathe kumunamiza Mulungu.

mphamvu yawo.

-Mukakhulupilira mwa Yesu, Iye akupulumutsani inu ku mphamvu ya ziwanda.

-Kodi Yesu anazilamula chiyani ziwanda?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:12

12-Koma anayilamulira kuti isamuwulule Iye.

-Yesu anazilamula ziwanda kuti zisamuwuze wina aliyense zakuti Iye ndi ndani?

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanafune kuti ziwanda zimuwuze wina aliyense za Iye?
-Yesu ankafuna kuti anthu amukhulupilire Iye chifukwa cha mawu Ache, Mulungu amafunanso kuti ife tonse timukhulupilire Iye chifukwa cha Mawu Ache.

-Yesu atatha kuchiza anthu, anapita pa phiri.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:13-19

13-Kenako Yesu anakwera m'phiri, nadziyitanira iwo amene anawafuna Iye mwini, ndipo anadza kwa Iye.
14-Ndipo anasankha anthu khumi ndi aŵiri kuti akhale ndi Iye, kuti akaŵatume kulalikira,
15-ndiponso kuti akhale nawo ulamuliro ochotsa ziwanda.
16-Aŵa ndiwo khumi amene anasankhidwa: Simoni (amene anamutcha kuti Peturo;
17-Yakobo mwana wa Zebedayo, ndipo Yohane m'bale wache wa Yakobo, (iwo amene anaŵatcha kuti Bowanege, kutanthawuza kuti ana a bingu);



-Chifukwa chakuti a Farisi sankasangalala ndi Yesu, ankamuyang'anitsitsa kwambiri Iye kuti amuwone ngati angaswe lamulo limodzi mwa malamulo a Mulungu.
-Yesu anakakhala kuti waswa lamulo limodzi mwa malamulo a Mulungu, a Farisi anakamulamula kuti aphedwe.

-Kodi Yesu anakaswa lamulo ngakhale limodzi mwa malamulo a Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi Yesu anasunga malamulo onse a Mulungu?
-Inde.

-Kodi Yesu anachimwako?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi olungamika kwambiri.
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu sanabadwe ndi tchimo.

-Yesu anamumvera Mulungu Atate mu china chilichonse.

-Pamene Yesu ankamumvera Mulungu, sanaŵamverenso a Farisi

-Kodi chifukwa chiyani Yesu sanaŵamvere a Farisi?
-Chifukwa chakuti a Farisi anaŵasintha malamulo a Mulungu.
-Kodi a Farisi anaŵasintha bwanji malamulo a Mulungu?
-Anawonjezera malamulo awo pa malamulo a Mulungu.

-A Farisi atawonjezera malamulo awo pa malamulo a Mulungu, anaŵapangitsa malamulo a Mulungu kukhala bodza.

-Limodzi mwa malamulo amene a Farisi anawonjezera pa malamulo a Mulungu linali lakuti pasapezeke wina ochiritsa munthu wina pa tsiku la Sabata.

-Kodi chifukwa chiyani a Farisi anawonjezera lamulo limeneli pa malamulo a Mulungu?
-Chifukwa chakuti ankati kuti kuchiza munthu wina ndi kugwira ntchito, ndipo Mulungu sankafuna kuti iwowo adzigwira ntchito la Sabata.

-Lamulo limene analiwonjezera a Farisi anaŵapangitsa malamulo a Mulungu kukhala bodza.

-Tsiku lina la Sabata, Yesu anapita mu sunagoge.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:1-2

1-Mu nthaŵi ina yache [Yesu] analoŵanso mu sunagoge, ndipo munthu wa dzanja lache lopuwala anali m'menemo.
2-[Afarisi] ankamufunira chifukwa Yesu chakuti am'mangire, chomcho ankamuyang'anitsitsa kwambiri kuti amuwone ngati angamuchiritse munthuyo pa tsiku la Sabata.

-Pamene Yesu anakaloŵa mu sunagoge, munthu opuwala dzanja anali momwemo.

-Kodi chifukwa chiyani a Farisi ankamuyang'anitsitsa kwambiri Yesu?



-Yesu ndi opambana kuposa anthu onse.

-Kodi ziwanda zinati chiyani zitamuwona Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:11

11-Ndipo mizimu yonyansa imene inamuwona Iye, inamugwadira, niyifuwula kuti, "Inu ndi Mwana wa Mulungu."

-Kodi ziwanda zinamutcha Yesu kuti ndani?
-Zinamutcha kuti Mwana wa Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani ziwanda zinamutcha Yesu kuti ndi Mwana wa Mulungu?
-Chifukwa chakuti zinadziŵa kuti Yesu anachokera kwa Mulungu Atate.

-Ngakhale kuti anthu sankadziŵa kuti Yesu anachokera kwa Mulungu Atate, ziwanda zinkadziŵa kuti Iye ndi Mulungu Mpulumutsi.

-Kodi ziwanda zinadziŵa bwanji kuti Yesu anali Mulungu?

-Ziwanda zisanalakwe ndikumutsata Satana, zinali angero abwino kwambiri ndipo ankamutumikira Yesu kumwamba.

-Ziwanda zonse zinkadziŵa kuti Yesu ndi Mulungu.

-Ngakhale ziwanda sizifuna kuti inu muzikhulupilira mwa Yesu.
-Ziwanda sizifuna kuti inu mudzikhulupilira Yesu chifukwa chakuti sizikufuna kuti inu mupulumuke ku

8-Zimene ankachita [Yesu] zitamveka, anthu ambiri a ku Yerusalemu, Idumeya, ndi aku tsidya lina la Yolodani, ndi a kufupi ndi ku Turo ndi Sidoni, anamutsata Iye.

-Anthu ambiri anapita kwa Yesu.

-Anapita kukamvera kuphunzitsa kwa Yesu.
-Anapita kukachizidwa ku matenda awo.

-Anadziŵa kuti Yesu ankatha kuchiza anthu.
-Mulungu yekha ndi amene amatha kuchiza anthu.

-Chifukwa chakuti anthu ambiri ankapita kukamuwona Yesu, nthaŵi yomweyo panali khamu la anthu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:9-10

9-Chifukwa cha khamulo [Yesu] anaŵawuza ophunzira ache kuti kangalaŵa kakhaliretu kokonzeka, kuti khamulo lisamukanikize Iye.
10-Pakuti adaŵachiritsa anthu ambiri, chomcho onse amene anali ndi zowawa anankanikiza Iye kuti akamukhudze.

-Anthu ambiri odwala ankapita kwa Yesu, ndipo ankachizidwa pongamukhuza Yesu.

-Chifukwa chakuti anthu ambiri ankakankhana kuti angomukhuza Yesu , Yesu anaŵawuza ophunzira ache kuti kangalaŵa kakhale kokonzeka kuti mwina mwache anthu angamukankhile Iye m'madzi.

-Panalibenso wina ofanana ndi Yesu.



-Ankafuna kuti awone ngati Yesu angamuchize munthu opuwalayo pa tsiku la sabatalo.

-Kodi Mulungu anakakwiya ndi Yesu anakamuchiza munthuyo pa tsiku la sabatalo?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanakakwiya ndi Yesu anakamuchiza munthuyo pa tsiku la sabatalo?
-Chifukwa chakuti kumuchiza munthu wina pa tsiku la sabata si ntchito, ayi.
-Chifukwa chakuti Mulungu Atate anafuna kuti Yesu amuchize munthuyo.

-Kodi Yesu anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:3-5

3-Ndipo Yesu anati kwa munthu wa dzanja lopuwala uja, "Imilira patsogolo pa anthuwa."
4-Kenako Yesu anaŵafunsa anthuwo kuti, "Kodi choloredwa ndi chiti pa tsiku la Sabata: kuchita chabwino kapena kuchita choyipa, kupulumutsa moyo kapena kupha?" Koma anthuwo anakhala chete.
5-Ndipo [Yesu] anaŵayang'ana ndi mkwiyo, anamva chisoni chifukwa chakuwuma kwa mitima yawo, kenako anati kwa munthuyo, "Tambasula dzanja lako." Analitambasula ndipo linachila.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anakwiya kwambiri ndi a Farisi?
-Chifukwa chakuti anayiwona kuti mitima yawo inali yowuma kwambiri.

-Kodi Yesu anadziŵa bwanji kuti mitima yawo inali

yowuma kwambiri?
-Yesu akhoza kuwona mu mtima mwa munthu wina aliyense.
-Yesu amawudziŵa mtima wa munthu wina aliyense.

-Yesu anayiwona mitima ya a Farisi kuti siyinkafuna kumvera zimene Mulungu ankaŵaphunzitsa.

-Ndikulakwa kwambiri kusafuna kumvera ku zinthu zimene Mulunu akutiphunzitsa ife.

-Farawo sankafuna kumvera ku zinthu zimene Mulungu ankamuphunzitsa iye, ndipo Mulungu anamulanga iye ndi imfa.

-A Isilayeli sankafuna kumvera ku zinthu zimene Mulungu ankaŵaphunzitsa m'chipululu muja, ndipo Mulungu anaŵalanga ndi imfa.

-Mulungu adzaŵalanga anthu amene sakumvera zimene Iye akuphunzitsa.

-Kodi Yesu anamuchiza munthu opuwala dzanja uja?
-Inde.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kumuchiza munthu opuwala dzanja uja?
-Mulungu.

-Kodi Yesu anamuchiza bwanji munthu opuwala dzanja uja?
-Anangolankhula.

-Kodi pachiyambi, Mulungu analenga bwanji dziko la pansi?



-Anangolankhula.

-Yesu anachiza munthu opuwala dzanja uja pongolankhula chabe ngati m'mene Iye analengera dziko la pansi pongolankhula chabe.

-Kodi a Farisi anachita chiyani Yesu atamuchiza munthu opuwala dzanja uja?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:6

6-Ndipo Afarisi anaturuka ndikuyamba kukhalira upo ndi a Herodi wakufuna kumupha Yesu.

-A Farisi anaturuka mu sunagoge muja ndi kuyamba kupanga upo wa m'mene angamuphere Yesu.

-Kodi a Farisi ankapanga upo ndi ndani kuti amuphe Yesu?
-A Herodi.

-Kodi a Herodi anali ndani?

-Anali anthu amene ankamutsata mfumu Herodi.
-Sankakhulupiliranso kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi.

-Mfumu Herodi imeneyi inali mwana wa mfumu Herodi amene ankafuna kumupha Yesu pamene Iye anali mwana.

-Kodi anthu anachita chiyani atamva za zozizwitsa zimene Yesu ankachita?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 3:8